

Abrahamu ndi Isake

Mogwirizana ndi Uthenga wa Mulungu:
Génesis 22:1-18



Cilankhulidwe: CiNyanja

Mulungu anaitana Abrahamu:
—Abrahamu!

Iye anabvomera: —Ndiri pano.

Mulungu anati: —Tenga Isake, mwana wako, okondedwa wako. Ine ndikakuonetsa kuphiri limodzi. Pita kuphiri limenero. Pereka mwanayo monga msembe yopsereza.

Mwana wace, Abrahamu anapita ndi Isake ndi ancito awiri. Patsiku lacityatu Abrahamu anati: —Khalani pano. Ine ndi mwana tikupita uko. Tikupita kukapembedza Mulungu.

Mwanayo anati: —Inu bambo, irikuti nyama (kapena nkhosa) ya nsembe yopsereza?

Abrahamu anabvomera: —Mulungu atipatsa.

Abrahamu anapanga guwa. Iye anaika Isake pamwamba pa guwa. Ndipo anatenga mpeni nafuna kumupha.

Koma panthawi imeneyo analankhula kumwamba.

Ngero wa Mulungu wa muyaya anati:
—Abrahamu.

Abrahamu anati:
—Ndiri pano.



Ngero anati: —Usaphe mwana. Tsapano ndidziwa kuti umaopa Mulungu. Inde sunakane Mulungu cifukwa ca mwana wako yekha. Sunakhale osamvera.

Abrahamu anayang'ana mbali mwace. Iye anatenga nyama. Iye anapatsa nyama monga nsembe yopsereza. Mwana wako sanafe monga nsembe yopsereza.

Mulungu wa muyaya anati: —Ine ndiri wosangalala cifukwa iwe unacita zimenezi. Iwe ndironjeza ndi kudalitsa kwambiri: Ana ako adzukulu ako ndi adzukulu adzukulu ako



adzakhala ambiri. Iwo adzagonjetsa adani awo. Ine ndidzakudalitsa. Ndidzadalitsa anthu a dziko lapansi cifukwa ca iwe. Iwe unacita cimene ndinakuuza.

("Kudzipereka" litanthauza kupha nyama ya msembe yoperekedwa kwa Mulungu.)

Yankhani mafunso:

- 1) Ndi ancito angati anapita naye pamodzi Abrahamu kuphiri?
- 2) Yankha dzina la cida cimene cinakagwiritsira ncito pakupha Isake?
- 3) Ndani analankhula kwa Abrahamu kuti asaphe Isake?
- 4) Lankhula mau ocepa kwa zimene waphunzira?
- 5) Nciani kudzipereka kwa thuntu?

Ficha Técnica:

Título: Abrahamu ndi Isake
(Abraão e Isaac)
(Abraham and Isaac)

Língua: Cinyanja

Primeira edição electrónica, 2010

Produzido por: Wycliffe SA
lidemo.net@gmail.com
C.P. 652
Nampula, Nampula
Moçambique

O utilizador pode copiar e distribuir a obra

